

Why did Jesus Die?



1. Because we are all sinners!

Mark 2:17 Ndipo pamene Yesu adamva ichi, adanena nawo, Wolimba safuna sing'anga, koma wodwala ndiwo; sindidadza kudzayitana wolungama, koma wochimwa kuti alape.

Aroma 3:10 “Monga kwalembedwa, palibe m' modzi wolungama, inde palibe m' modzi;”

Matthew 18:11 Pakuti Mwana wa Munthu adadza kudzapulumutsa chotayikacho.

2. Because there is a cost for your sin!

Matthew 15:18-20 Koma zotuluka m'kamwa zichokera mumtima; ndizo ziyipitsa munthu.

Pakuti mumtima muchokera maganizo woyipa, zakupha, zachigololo, zachiwerewere, zakuba, za umboni wonama ndi zamwano. Izi ndizo ziyipitsa munthu, koma kudya osasamba manja sikuyipitsa munthu ayi.

Aroma 6:23 “Mphotho yake ya uchimo ndi imfa,

Mark 16:16 Amene akhulupilira nabatizidwa, adzapulumuka; koma amene sakhulupirira adzalandidwa.



There is a cost for your sin!

3. Because Jesus died and paid for our sins on the cross!

Matthew 1:21 Ndipo adzabala mwana wa mwamuna, ndipo udzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iye adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo.

Aroma 5:8 Mulungu amaonetsa chikondi chake kwa ife mu ichi: pamene tidakali wochimwa, Khristu anatifera ife.

John 3:16 Pakuti Mulungu adakonda dziko lapansi, kotero kuti adapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira mwa Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.

Matthew 18:11 Pakuti Mwana wa Munthu adadza kudzapulumutsa chotayikacho.

4. Salvation is a free gift, not by good works. You must take God's word for it, and trust Jesus alone!

Aefeso 2:8-9 Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo, mwa chikhulupiliro – ndipo ichi chosachokera kwa inu, chili mphatso ya Mulungu – chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense.

Titus 3:5 Zosati zochokera m`ntchito za m`chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake adatipulumutsa ife, mwakutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe atsopano a Mzimu Woyera:

Acts 4:12 Ndipo palibe chipulumuso mwa wina yense: pakuti palibe dzina lina pansu pa thambo la Kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo.

5. We must put our faith and trust in Christ alone!

Mark 9:23 Ndipo Yesu adanena naye, Ngati mukhulupilirira, zinthu zonse zitheka kwa iye wokhulupirira.

Mark 1:15 Nanena, nthawi yakwanira ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; lapani, khulupirirani Uthenga Wabwino.

Mark 10:15 Indetu ndinena ndi inu, munthu ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse.

Aroma 10:9,10,13 Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako, Ambuye Yesu, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu adamuwukitsa kwa akufa, udzapulumuka. Pakuti ndi mtima munthu akhulupirira kutengapo chilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo chipulumutso. Pakuti amene aliyense adzayitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.



Put your faith in Christ alone!

Inde, ndikosavuta! Simungalandire chikhululuko kuchokera kwa Mulungu. Simungalipire chifukwa cha kukhululuka kwanu kuchokera kwa Mulungu. Mukhonza kungolandira, mwa chikhulupiliro, kudzera mwa chisomo ndi chifundo cha Mulungu.

Ngati mukufuna kulandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wanu ndikulandila chikhululuko kuchokera kwa Mulungu, ili ndi pemphero limene mungapemphere. Kunena pemphero ili kapena pemphero liri lonse sikungakupulumutseni. Ndikukhulupilira mwa Yesu kokha kumene kungakupulumutseni ku machimo. Pemphero ili ndilongosonyeza kwa Mulungu chikhulupiliro chanu mwa Iye ndikumuthokoza pakukupatsani za chipulumutso chanu.

“Mulungu,

ndikuzindikira kuti ndakulakwirani ndipo ndili oyenera chilango. Koma Yesu Khristu anachitenga chilango chimene chinali choyenera ine kotero kuti mwa chikhulupiliro mwa Iye ndikhonza kukhululukiridwa. Ndikuyika chikhulupiliro changa mwa inu kuti ndikapulumuke. Zikomo chifukwa cha chisomo chanu chodabwitsa ndi kukhululuka kwanu! Amen!”